Uzimu Weniweni - Zolembedwa mu Chichewa

Gawo 6: Momwe Mungagonjetsere Choipa Zolunjika kwa Inu

Zolembedwa ndi Chip Ingram

Pomwe tikuyamba, ndikufuna kukufunsani kuti mupite ku malo amene simungawakonde kwenikweni kupitako, koma ndikuwuziranitu kuti ndi kwa phindu. Ndikufuna mutsamire mmbuyo pang'ono muganizire mobwereza, ndipo ndikufuna kuti muyankhe funso ili mmutu mwanu. Khalani omasuka kutseka maso anu kwa kamphindi ngati zili zothandiza.

Pa anthu onse mmoyo wanu mpaka lero amene munganene kuti anakupwetekani kwambiri amene akubwera mmaganizo mwanu? Kodi ndi ndani amene anakupatsani chilonda? Amene ananama zokhudza inu? Amene anakuchokerani? Amene anatenga ndalama zanu? Amene anakunenani miseche? Amene anakuchita nkhanza zokhudza kugonana muli mwana? Amene anakhala osayamika ndi amene anakuchititsani manyazi kugulu la anthu? Amene ananena zinthu ku nthawi yosanthula Baibulo kapena ku tchalitchi amene anabweretsa kuwawa ndi kusagwirizana kwakukulu, ndipo inu munakhala munthu wolakwa? Ndi ndani anakupachikani?

Mwamva kodi? Sindikufuna kukukokani chipsera sindikutanthauza kuwutsa zinthu- kwa ambiri a inu, zina mwa zinthu izi zinapsinjika pansi pa mtima. Ndikufuna munditsatire, ndipo ndikufuna kuwerenga kwa inu chimene ndikuganiza kuti ndi mawu a mphamvu kwambiri anatulukako mkamwa mwa munthu amene anayendako pa dziko lapansi. Mawuwo ndi odziwika kwa ena mwa inu chimene ndi chinthu chatsoka chifukwa amatha mphamvu zawo.

Kotero monga ndikuwerenga awa, ndikufuna inu muganizire za munthu amene anakupatsani inu chilonda, koma ndikufuna muganizire kuti zikadakhala zotani ngati inu mukadamakhala mudziko lodzadza ndi katundu wanu akutengedwa kuchoka kwa inu, ndipo mukukanidwa ndi anthu a pa banja lanu, zonse chifukwa chakuti mukukhulupirira kuti mlaliki woyendayenda uyu anali, pamenepo, Mesiya - Mulungu-munthu amene anabwera kudzapulumutsa dziko lapansi- ndipo munadziwa kuti munasowekera kumutsatira Iye. Ndipo ngati chotsatira chake, chilichonse kuchokera ku chizunzo, kuyendetsedwa mubwalo la milandu, kuchotsedwa mu banja lanu la Chiyuda. Yesu akanayankhula mawu awa kwa iwo, ndipo pano pali mawu amene iye akunena kwa ife.

Mateyu Mutu 5 mu Ulaliki wa pa phiri. "Munamva kuti kunanedwa, Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako; koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu ndi kupempherera iwo akuzunza inu." ndiye kenako akupereka chifukwa chiyani. "Kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa Kumwamba chifukwa Iye amakwezera dzuwa lache pa oipa ndi pa abwino, namavumbitsira mvula pa olungama ndi pa osalungama. Chifukwa kuti ngati muwakonda akukondana ndi inu mphotho yanji muli nayo? Kodi angakhale amisonkho sachita chomwecho? Ndipo ngati mulankhula abale anu okhaokha, muchitanji choposa ena? Kodi angakhale anthu akunja sachita chomwecho? Mukhale angwiro. Mawu ndi kukhwima "teleios". Awa ndi mawu athu a kukhwima. Ndi nzeru za chinthu china kapena munthu wina kukwaniritsa chilengedwe chenicheni. Khalani okhwima. "Mukhale angwiro monga Atate anu a Kumwamba ndi angwiro."

Tsopano pamene mukutenga cholembera chanu ndi kutenga zolemba zanu, ndikufuna mulembe chinachake chifukwa musowekera kuti mumvetsedi ichi. Sikovuta kukhala Mkhritsu wa Aroma 12. Chotsani zimenezo mmaganizo anu. Ena mwa inu mukuganiza kuti ndi zovutitsitsa kwambiri… kugonjera kwa Mulungu, ndi kupatuka kuchoka ku zopindula za dziko lapansi. Sizovuta. Ndi zosatheka. Lembani mawu

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

amenewa. Ndi zosatheka chifukwa ngati simukuganiza kuti ndi zosatheka, mudzayesera kukhala mmodzi. Ndipo mudzayesera kukhala mmodzi kuchokera ku mphamvu za inu eni nokha, ndi thupi lanu ndi nyonga zanu ndi kudziletsa kwanu, ndi mphamvu za chifuniro chanu. Ndipo anthu amene ndi ochita bwino pa ichi amatchedwa Afalisi. Ndipo Aroma 12 sanalembedwa kukuthandizani inu mu mphamvu zanu kapena mumphamvu zanga kukhala ndi lamulo la makhalidwe lolimba. Inali mbiri. Inali chinthunzi. Inali chithunzithunzi cha chimene chingachitike kwa munthu pomwe akukumana ndi chifundo ndi Chisomo cha Aroma Mutu 1, 2, 3, 4, 5, 6, 7, 8, 9, 10 ndi 11. Ili ndi yankho la chikhulupiriro.

Dziwani mu zolemba zanu. Akhristu a pa Aroma 12 amalunjika pa ubale, osati pa malamulo kapena zochitika za chipembedzo. Sizikutanthauza kuti palibeso malamulo ena alionse ndipo sakutanthauza kuti ngati wotsatira Yesu palibepo zochitika za chipembedzo, koma lingaliro lililonse la lamulo kapena zochitika za chipembedzo ndi kudzutsa ubale ndi Mulungu, ndiponso ubale wanga ndi anthu - ngakhalenso ubale wanga ndi ine mwini wake - munjira yathanzi. Ndithu, mungathe kufotokoza mwachidule kwa Akhristu a pa Aroma 12- cholinga chawo chawo chachikulu - cholinga chathu chathu chachikulu - ndi chikondi. Mukudziwa, pomwe Yesu anafunsidwa kodi lamulo lalikulu kuposera onse ndi liti, mukukumbukira chimene Iye ananena? Kondani Ambuye Mulungu wanu. Bwanji? Ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi nzeru zanu zonse, ndipo ndi mphamvu zanu zonse. Ndipo chinanso ndi chiyani? Chiyaninso? Ndipo kondani anzanu monga mudzikondera inu eni.

Ngati mungatenge chilichonse mu Aroma 12 monga timachita kungodutsamo msanga pano kotero kuti tisayiwale chimene takamba kale maphunziro awiri kapena atatu kapena anayi apitawo. Aroma 12 ndi chinthunzithunzi cha mtumwi Paulo kulingaliranso pa chiphunzitso cha pa phiri ndi mtumwi Paulo, kulingaliranso za kukambirana kwake ndi Khristu woukitsidwa mu Arabia. Yesu anawawuza iwo kukonda Mulungu kukonda iwo eni ake, kukonda ena, ndipo Paulo ndi wanzeru kwambiri, munthu wophunzira kulembera ku gulu la ku Aroma, ndipo akudziwa ziyenera kukhala zochitikadi. Ndiye kotero akuti ndiloleni ndikudziwitseni mmene zimaonekera kukonda Mulungu mmoyo wa tsiku ndi tsiku. Zikutanthauza kuti pa tsiku lina, pa nthawi ina, mutatha kulandira chisomo chake ndi kubadwanso muuzimu, kuti mudzanena kwa Mulungu “Ndikugonjera zonse. Ndili mu zonse” chifukwa chimenecho ndicho kutumikira kwa uzimu kumene Mulungu amakhumba ndi ichi ndi chimene akutanthauza kukonda Mulungu.

Ndipo akuti pali mpikisano wa chikondi chimenecho. Kumbukirani mayendetsedwe a dziko lapansi amene amafuna kukunyengani inu, ndikukuwuzani inu kudzera mu chilakolako chathupi, ndi chilakolako chamaso, ndi madama a moyo amene ndi ofunikiradi, ndi kupambana kwenikweni, ndi mphamvu zenizeni, ndi chikondwerero chenicheni chidzabwera? Ndipo akuti muyenera kukana chikondi cha dziko lapansi. “Ngati munthu wina akonda dziko lapansi chikondi cha Atate sichili mwa iye.”

Ndiye kenako mundime 3 mpaka 8, anakamba zokhudza kukonda inu eni. Osati kungoyang’ana pa kalilore ndi kunena ndine woumbidwa moopsa ndi modabwitsa koma kuyang’ana pa kalirole wa mtima wanu kudzera mmaso a Mawu a Mulungu ndi kunena, “Ndine wokhululikidwa. Ndine wotengedwa ngati mwana wake. Ndili ndi Mzimu wa Mulungu wa Moyo mkati mwanga. Ndinamatidwa. Ndili ndi mphatso za uzimu. Ndine chinthu cha chikondi chake. Ndili mwa Khristu. Mulungu Atate tsopano amaona ine munjira yofanana ndi mmene amawonera Mwana Wake Yesu. Ndine wolungama mmaso Mwake uku ndikudziunikanso modekha, komabe mudziko lakugwa.

Zimachokera kokonda Mulungu, ndikusakonda dziko lapansi, ndi kukonda inu eni ake kufika kokonda banja, thupi la Khristu. Kuyamba kutumikirana mwamphamvu wina ndi mnzake. Ndiye kenako mapeto ake, tidzakamba mu phunziro ili, kodi zimaoneka bwanji muzochitika za kukonda adani anu?

Tsegulani ma Baibulo anu ku Aroma 12. Ndimazikonda pomwe mukutsegula Baibulo chifukwa ndi Maw a Mulungu osangoti ndi pepala chabe. Ndikutanthauza, ndi mawu omwewo, koma pamakhala maganizo akuti pomwe mwatsegula Baibulo lanu ndi kuwerenga ilo, kuli ngati mukudziwa china chake? Izi ndi za umwini.

Akuyamba kutiwuza momveka bwino mmene tingayankhire ku zoipa zimene zalunjika kwa ife mu ndime 14. Mu ndime 14 mpaka 16, akutipatsa ife lamulo labwino. Umu ndi mmene mungayankhire kwa munthu ameneyo akubwera ku maganizo anu pomwe ndinayamba uthenga uwu ndi kukufunsani kuti muganizire za munthu amene anakupwetekani iye adzanena kuti umu ndi mmene muyankhire munthu ameneyo. Ndipo ndikuchenjezani zidzaoneka zomveka mopusa ndi zosatheka.

“Dalitsani iwo akuzunza inu; dalitsani, musawatemberere. Kondwani nawo iwo akukondwera; lirani nawo akulira. Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzache. Musasamalire zinthu zazikulu, koma phatikanani nao odzichepetsa, Musadziyesere anzeru mwa inu nokha.”

Akunena kuti mukusowekera kuwadalitsa iwo. Kenako akupereka lamulo loyipa. Pali mayesero pomwe adani athu ndi anthu amene anatipweteka ife ndipo iye akulankhula mwachindunji. Ndime 17. “Musabwezere munthu alliyense choipa chosinthana ndi choipa. Ganiziranitu zinthu za ulemu pamaso pa pa anthu onse. Ngati nkutheka, monga momwe mukhoza, khalani ndi mtendere ndi anthu onse. Musabwezere choipa, okondedwa, koma patukani pa mkwiyo; pakuti kwalembedwa, Kubwezera kuli kwanga, Ine ndidzabwezera, ati Ambuye.”

Mosiyanitsa. Pano pali mmene mungamuchitire munthu ameneyo ali mmaganizo anu. “Koma ngati mdani wakoo akumva njala, umdyetse, ngati akumva ludzu, ummwetse; pakuti pakutero udzaunjika makala a moto pa mutu pache.” Ndipo izi sizikutanthauza kuti Mulungu adzawapweteka iwo. Tiphunzira posachedwapa kuti kwenikweni zikutanthauza chiyani.

Kenako pali zotsatira zauzimu. Pali chinthu ichi chimene pomwe mwachita munjira imene Yesu anachitira kwa adani ake. Yesu amakhala mwa inu mwa Mzimu Wake ndipo mmachita ndi mphamvu za Mawu Ake ndi mmudzi weniweni. Akunena kuti, “Musagonjetsedwe ndi choipa. Ndipo timakhala mudziko loyipa. Koma akuti pali china chake chimene ndi champhamvu kwambiri kuposera choipa “Gonjetsani choipa ndi chabwino.”

Munthawi yathu yotsarayi, ndikufuna ndiphwanye mwachindunji ndi mothandiza mmene zimaonekera monga ngati kudalitsa iwo amene amakuzunzani inu. Ili ndi lamulo loyamba ndi labwino. Ndipo lamulo ndi ili “Dalitsani iwo amene akuzunza inu.” Ichi ndi chimene munayitanidwira kuti muchichite mu ndime 14, 15 ndi 16, Akupatsani njira zitatu zachindunji za mmene mungawadatsire iwo.

Mawu akuti dalitsa, sali ngati pamene wina wake wayetsemula, ndipo inu ndi kunena, udalitsike iwe. Sizili choncho ayi, chabwino? Mawu awa makamaka akutanthauza kukhumba chipulumutso cha munthu wina. Kutanthauza khumbo ndi kulakalaka kwa madalitso a Mulungu ndi kukondwera kukhala pa iwo. Zitanthauza kuti, kwa mdani ameneyo, kuti moyo wawo uyende bwino. Ngatia li pa banja, banja lawo liyende bwino ndithu. Ngati ali makolo, ana awo achite bwino. Ngati ali pa ntchito, akhale opambana. Uwu ndi mdalitso. Ichi ndi chimene mukupempherera.

Ndipo pomwe akunena kuti anthu amene akukutembererani inu, awa sianthu akuti akungogwiritsa ntchito mawu otemberera okha kwa inu. Lingaliro la mawu awa “dalitsani iwo amene akutemberera inu”, ndi anthu amene amakuchotsani mocheza chifukwa cha chikhulupiriro chanu. Ndi anthu amene mwa mawu otuluka mkamwa mwawo amakuchepsani chifukwa cha chikhulupiriro chanu. Ndi anthu amene muzaka zoyamba za mmazana mu malo ambiri kuzungulira dziko lonse lapansi, anthu amene amakudulani inu, amakuzunzani ndi kufuna kukuphani chifukwa inu ndinu wotsatira wa Khristu. Akunena kuti, ndikufuna muwadalitse iwo.

Pali pali magawo atatu. Gawo loyamba ndi kudalitsa ena ndi kuwakhululukira iwo. Kukhululukira iwo ndi kovuta. Ngati mungapempherere, mdalitso, chipulumutso chawo, ndipo ngati mukufuna Mulungu awakhululukire iwo, mukudziwa chiyani? Muyenera kuwakhululukira iwo. Ndipo inu mukudziwa kachidutswa kena mu ndie ya pemphero la Ambuye? “Tikhululukireni ife machimo athu monga ifenso tiwakhulukira ena.”

Mfungulo wokondera adani anu ndi wakuti inu ndi ine tifike pa mulingo wakuti tikumvetsetsadi mmene Mulungu alili ndi chifundo ndi kuti Mulungu sanatipatse zimene ife zikutiyenera. Musowekera kuyang’ana pa zolinga zanu za mmbuyomo, ndi zinthu zimene mwachita ndi zimene mwamudandaulira Mulungu - “oh Mulungu, chonde, chonde musalole ndilandire zotsatira za izi. Oh Mulungu, nditoleni ndi kundiyeretsa ine.” Ndipo iye wachita. Ndiye kenako chimene anganene ndi, “Ndikufuna iwe kuchitira munthu uyo zimene ndakuchitira iwe.”

Tsopano anthu ambiri amasokonekera pakafika pa kukhululuka chifukwa amandiuza zinthu monga ngati chabwino, mwamuna wanga anandithawa. Sakupereka thandizo lina lililonse la ana. Kapena, abwana anga akakhala akufuna azindigona mwankhanza ndipo ndinapita kwa amene amalemba ndi kuchotsa anthu ntchito ndipo, sanandithandize ine, ndiye ndikukhala mmoyo umenewu, ndipo nthawi zonse zimene achitira ndemanga- ndimamukhululukira, koma ndimakhala okwiya. Kotero mmathana nako bwanji kukhululuka kotere?

Kapena wina wake mmoyo wanga anandigonapo mwankhanza, ndipo ndinawakhululukira iwo ka 144, ndiye kenako masana a la Mulungu lina lake lamya inalira, ndipo ndikuganiza kuti akhoza kukhala iwo, ndiye ndimamva kugubuduzika mmimba mwanga ndipo mkwiyo uwu…

Chikhululukiro chiri ndi magawo atatu. Lembani izi chonde. Gawo loyamba ndi chisankho chokhululuka. Sizakumva mmene zilili. Lilibe kanthu ndi zakumva zanu za mthupi. Ndi chisankho. Pakutha pa nthawi yathu pamodzi, ambiri mwa inu mutsegula gawo mu Baibulo mwanu ndi kunena kuti ndamukhululukira munthu uyu lero, ndipo mulembe tsiku chifukwa ndi chisankho.

Chachiwiri ndi ndondomeko ya chikhululukiro. Kotero, inu mukhululukira, ndipo muyenera kupitiliza kukhululuka. Uwu ndi ulendo umene zakumva za mthupi mwanu zimagwirizana ndi chisankho chimene mwachita chifukwa mungathe kukhululuka ndipo mawu akuti khululuka, akutanthauza kumasula kapena kutaya.

Mwamawu ena, ndikutengerani khumbo langa kwa iwo kuti ndilipidwe, ndipo ndi wamasula iwo ku chimenecho monga ngati mmene Mulungu anandimasulira. Ndipo kotero sindidzayankhulanso chili chonse choipa chokhudza iwo. Sindidzawafuniranso zoipa iwo. Ndiwatulira kwa Mulungu, ndipo ndidzawakhululukira iwo monga mmene Mulungu anakhululukira ine: mwaulele.

Ndi chisankho. Koma ndiye, pomwe anawataya ana amenewo, ndipo anawadyetsera zowopsa ana zokhudza inu kapena mukulandira kalata iyi mu positi ofesi, ndipo mukumva zokhudza mnyamata uyu amene anandibera mulu wa ndalama ndipo iye ali ku tchuti ku Hawaii, kapena munawerenga za iye mu Forbes, ndipo zimakupengetsani. Kodi zimatanthauza kuti simunakhululuke? Ayi. Zikutanthauza kuti muli pa ulendo. Ndipo ulendo ukutanthauza kuti pomwe mukudalitsa, mumayamba kuwapempherera iwo.

Pomwe ndinayamba kukumana nazo ndinanyengezeredwa munjira yopweteka kwambiri, munjira yokhumudwitsa kwambiri, ndipo ndinagoma ndipo sindinathe kuturukamo. Ndinali ndi mnzanga amene anayenda nane munjirayi ndikundiphunzitsa ine mmene ndingachitire izi. Ndipo kotero ndinayamba kupemphera. Ndi mapemphero anga moonadi mtima amayamba motere: Okondedwa Mulungu, mumupatse munthu ameneyo chimene chiyenera iye.

Ndikutsimikiza. Kunali ngati Atate wakumwamba, mutengani uyu, mukudziwa? Ndipo pamene ndinapitiliza kupemphera, Mzimu Woyera amagwira ntchito, koma chimenecho sichinali ndendende chokhudza chimene mdalitso uli.

Koma mbali ina ya icho, ndi chakuti mukusowekera kukhala weniweni mu zakumva zanu za mthupi kwa Mulungu. Ndikuganiza kuti anthu amaganiza, Mulungu ali ndi chipinda choyeretsedwa. Ndili ndi nkhani ya inu. Akhoza kuthana ndi china chili chonse chimene mungabweretse, ndipo chimene iye angayamikire ndi uweniweni. Ndipo nthawi zina ndi zopweteka ndipo ndi zokukuta. Werengani Masalmo.

Potsiliza mapemphero a ine anakhala ... “Oh, Mulungu, mungomuthandiza iye kuwona mmene analakwira ndi kumubweretsa iye…?” Ndipo nthawi iliyonse ndinamva zokhudza iye, mkwiyo uja umabwera. Ayi, ndinamukhululukira, koma ndipitilizabe ndondomekoyo. Ndipo mizeyi iwiri kapena itatu itatha ndinayamba kupemphera… “Mulungu mudalitse banja lake?”

Ndinatsimikiza kuti pa mgonero uliwonse wa Ambuye --sindidzadya mgonero wa Ambuye mpakana nditapemphera moonadi ndipo kuchokera mumtima mwanga kudalitsa munthu ameneyu mumoyo wake, mubanja lake, ana ake. Ndipo zonse zimene ndingakuwuzeni ndi zakuti kwa nthawi yayitali sanasinthe, sindikukhulupirira, koma ndinachitadi.

Pamakhala ululu mumtima mwanu pomwe pali kuwawidwa mmoyo wanu ndipo munapwetekedwa. Ndipo ngati wina wake mwanzeru ananena, pomwe tikukana kukhululuka, ndi kukhala ngati tamwa mwakhwala a poizoni ndipo tikuganiza kuti munthu winayo ndi amene amwalire. Ndikuganiza kuti pali chisokonekero chambiri chokhudza chikhululukiro, ndi zimene tikumva mthupi.

Kukhululuka ndi chisankho, ndiye kenako mumawadalitsa iwo, mumawapempherera iwo. Tiphunzira mu kamphindi simungopempherera iwo wokha, koma mumayamba kuwachitira zinthu zabwino adani anu enieni. Monga ngati ali ndi njala, mumawadyetsa. Ngati ali ndi ludzu mumawapatsa china chake kuti amwe. Pali njira zapadera zimene mumachita zinthu zabwino kwa anthu amene sakuyenera izo.

Ndikufuna muganizire za Yesu mmunda. Anafa ku khululukira inu ndi kukhululukira ine. Ndipo nthawi zina timaganiza za izi monga Yesu amandikonda, ichi ndimadziwa? Ndingakuwuzeni kachinsinsi? Iye sanamve ngati akufuna kukukhululukirani. Munayamba mwaganizako za izo? Ali mmunda; Akutuluka thukuta ngati nthuli za magazi kuchokera mutimabowo ta nthupi pa nkhawa imene anali nayo. Ndi Mulungu watunthu. Koma ndi munthu watunthu. Sanafe ngati Superman wa mu kanema okhala ndi S pa mtima pake koma akudutsa mmaganizo owawa. Monga munthu, Akanafa. Koma ngati Mulungu Mwana, Iye anadziwa

chimene apeze pa mtanda, tchimo lanu, ndi tchimo langa ndi tchimo la anthu onse a nthawi zonse ayikidwa pa Iye. Anakhala nsembe ya tchimo lathu.

Ndipo pa nthawi imene tchimo linadza pa Iye, Atate akanatembenuka. Ndipo kwa nthawi yoyamba muyaya, Atate ndi Mwana anasiyanitsidwa, ndipo iye anakumana nako kusiyanitsidwa ndi mphotho ya tchimo. Ndipo pamene ululu umafika, Iye anamenyedwa kwambiri mmoyo mwake, ndipo anachititsidwa manyazi, anavulidwa zovala, ndipo anali ndi chisoti chaminga, ndipo anawonetsedwa ku chigulu cha anthu. Ndipo kodi mukukumbukira chimene anapempherera? “Atate, lolani chikho ichi chidutse” Mukudziwa chimene Iye amanena? “Sindikufuna kuchita izi. Sindikumva ngati ndichite izi.”

Kukhululukira ndi kukonda sikuli ngati kumva chimene ukufuna. Ndi kusankha kupatsa munthu wina chimene iwo akusowekera kwambiri, pamene iwo sakuyenera, pa mtengo waukulu wa umwini. Ndipo pamene Mulungu akuti khululukirani munthu uyu, zonse zimene tikuchita ndi chakuti tikuponda mmapazi a Yesu. Kodi zikuwayenera iwo? Ayi kumene. Ngakhalenso ine. Ngakhalenso inu ndondomeko ya chikhululukiro ndi chisankho.

Chachiwiri kukhululuka - kukhululuka ndi ndondomeko, ndiye kenako kukhululukidwa kumachitika. Ndipo pano pali mmene mungadziwire pomwe kwachitika. Mungathe pompopompo kukondwerera pa madalitso a mmoyo wawo. Ndikadamapemphererabe ndondomeko ya kukhululuka. Iyi inali nkhondo yanga yeniyeni yoyamba, ndipo ndakhala ndi zochuluka chiyambire. Ndikulingalira kuti ukamakula mumapachikidwanso kwambiri ndipo zinthu zovuta zimabwera mmoyo mwanu. Mu zochitika ngati izi, patatha miyezi isanu ndi inayi ndisanadutsenso mu kupachikidwa kotero, ndipo ndimadya Mgonero wa Ambuye, ndipo ndimapempherera munthu uyu kuposera amayi anga chifukwa mkwiyo umatha kungobwera, ndipo nthawi ili yonse ndimaganizira za maganizo a mkwiyo ndimayamba kumupepherera, ndi kumudalitsa.

Panali nthawi ina yake, nditatsala pang’ono kulalikira munthuyu anabwera kwa ine nanena kuti, “oh, Kodi munamva za munthu uyu? Chinthu ichi chabwino zedi chamuchitikira iye: ndipo ine ndinachita chinthu chabwino cha Chikhristu ndi kunena kuti, “Ohoo, eya, zabwino kwambiri” koma mkati mwanga munali matenda ndi kukhumudwa. Ichi chinali choyipa kwambiri. Izi ndi zokondera. Atatha kuchita zimene anachita kuno zija, ndipo uko akudalitsika? Chabwino, ndaona sindinathe. Zaka ziwiri zitadutsa ndili mu tchalitchi, ndipo munthu akubwera kwa ine. Kodi munamva za munthu yemwe uja? Ndinanena kuti ayi. Iye ananena ichi, ichi, ndi ichi chimene chinamuchitikira munthu uja. Ndipo ndisanaganizire, ndi sanalingalire za chimene iye amanena munali chikondwerero. Ndinanena kuti “izo ndi zabwino kwambiri.” Ndinatsimikizadi. Ndinasiya kupempherera iye ndisanatumikire za mgonero wa Ambuye. Ndinali nditatha, Ndinali nditatha. Chikhululukiro ndi chisankho. Kukhululuka- ndondomeko imene zakumva zanu zimakwera ndi kutsika. Pamene ndi ndikudalitsa ndi kupemphera, ndimakhululuka. Zimachitika.

Ena mwa inu mutuluka mundende lero. Ena mwa inu mwakhala mukuzikankha pansi, ndi chifukwa chake inu muli wokhumudwa. Ena mwa inu mmadya pomwe mulibe njala chifukwa mwakhala mukukankhira pansi zinthuzi. Ena mwa inu muli ndi zilonda za mmimba ndi mutu wa ching’alang’ala, ndipo kuli zowawa zambiri za thupi ndipo gawo lalikulu la chifukwa chimene matupi athu sagwira ntchito bwino, ndi chifukwa timapanga zinthu zopanda nzeru, ndipo tili ndi zizolowezi zoipa zovuta kuzisiya. Zambiri za izi zazikika mizu mukusowa kwa chikhululukiro. Pololera kumasula anthu awa. Mutha kuyamba lero.

Chinthu chomaliza akuti, osati kungowakhululukira kokha, koma kuwamvetsetsa iwo. Ndipo kotero sikungokhululukira wina wake mmaganizo. Tsopano izi zayamba kupita kovuta kwambiri. Iye akuti “kondwerani ndi iwo akukondwera, ndipo lirani nawo ndi iwo akulira. Akhristu nthawi zambiri

timangotengera mawuwo, ndipo timaganiza kuti ndi mmene tikuyenera kuchitirana wina ndi mnzake. Inu simukusowekera lamulo lili lonse kukondwerera ndi anthu amene mumawakonda, ndipo simukusowekera lamulo lililonse la kulira ndi anthu amene akulira amene inuyo mumawakonda amene ali ndi matenda a khansa. Muwawo pano ndi awa a mmene tingadalitsire kapena kuchitira ndi adani athu.

Ndiye kotero, bwana amene anakung'ambani, amene anachita zinthu zowawa kwambiri kwa inu, amene anakuberani zimene inu munachita ndipo anthu ndikuyamikira iyeyo, kukakhazikitsa ku kampani ina, napita kugulu la anthu, ndikulemera kwambiri, ndipo inu munaluza ndiye mwakhala mukuziganizira mpaka kalekale kapena chibwenzi chimene chinakuthawani ndi kukakwatirana ndi munthu wina, ndipo tsopano ali pagombe mbali mwanyanja pamene inu mulibe ndalama. Izi ndi zenizeni mmoyo zoona? Ndiye kenako amapezeka ndi matenda a khansa, kapena apezeka pa ngozi ya galimoto mukudziwa zimene izi zikunena? Kondwerani ndi iwo amene akukondwera, ndipo lirani ndi iwo amene akulira.

Kodi chingachitike ndi chiyani ngati mutalowa mu chipinda cha chipatalacho ndi kunena kuti,"Ndikudziwa kuti kwatha zaka 5. Simungakhulupirire kuti ndakhala ndikukupemphererani." Simuyenera kuwawuza iwo chifukwa. "Ndikufuna inu mudziwe kuti ndakukhululukirani chimene munachita. Koma pomwe ndinamva za matenda awa a khansa, ndinamva kukakamizidwa ndi Mulungu kubwera kudzakuwuzani kuti Yesu amakukonda inu. Mungalole kuti ine ndikupemphereren tsopano lino?" Tangoganizirani iwo akukanda mutu wawo?

Kapena chinthu china chabwino chachitika kwa iwo, kukondwerera ndi iwo. Mukudziwa, mwina anakwatiranso. Ndipo ali ndi mwana, ndiye china chake chachitika, ndipo inu munawakhululukiradi iwo, ndipo mukupempherera kuti adalitsike iwo ndi banja lawo. Bwanji mutawalembera ka pepala ndi kunena, "Ndikuyamika Mulungu. Ndakhala ndikukupemphererani inu ndi banja lanu kwa zaka ziwiri, ndipo mukudziwa, ndi zosangalatsa kuwona madalitso awa pa moyo wanu."

Ndipo kwa ena… Pano pali chodzikanira. Ngati munagonedwapo mwankhanza, kapena anakupwetekani kapena munachita china chake, pali anthu ena amene simufunika kukhala okhudzidwa nawo. Koma mutha kuwatumizira mphatso yosayembekezeka chifukwa pano pali zimene zimachita. Zimasintha inuyo. Ndipo musanayambe kundiyanga'ana ine monga ngati izi ndi za misala zedi zimene simunamvepo, ichi sichimene Yesu anachita? Kodi Yesu sanabwere ku dziko limene Ake omwe sanamulandire iye koma anamukana iye? Kotero ndife adani a Iye, Paulo akadatiyitana ife. Pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifere ife. Aroma 5:8.

Ndiye kutero tikadali adani ake, anachita chiyani? Anapita ku ukwati kukakondwera nafe. Anadzutsa ana ang'ono kwa akufa. Anadyetsa a njala. Kapena ndi Lazalo, anachita chiyani? Analira. Onani, Yesu sananene kuti mukayeretsa zochita zanu, ndipo chili chonse chikayenda bwino, ndiye ndidzakukondani. Iye anakondwera ndi iwo akukondwera ndipo iye analiranso iwo amene akulira chifukwa ndi kukoma mtima kwa Mulungu kumene kumabweretsa kulapa.

Izi ndi zotsutsana kwambiri. Izi ndi zodabwitsa kwambiri. Pomwe inu, ndi mphamvu za Iye ndi chisomo chake, mwasankha kuchita ichi, china chake chimachitika, ndipo chisomo cha Mulungu chimagwira ntchito kudzera mwa inu. Anthu amayamba kukhulupirira kuti mwina mwake Yesu uyu ndi weniweni. Ndipo kenako zimayamba ndi kukhululuka. Ndiye kenako kuli kudzizindikira. Ndiye kenako dziwani gawo lomaliza la ndime 16. Iye akuti pano pali mgwirizano umene muyenera kukhala nawo mosamala kwambiri. Akuti, Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzache. Musasamalire zinthu zazikuru koma phatikanani nawo

odzichepetsa" - muzungulize mawu akuti "mugwirizane"- "ndi anthu amene ali ndi udindo wotsika". Ndiye kenako… "Musadziyesere anzeru mwa inu nokha."

Mudziko lakugwa, ndi anthu oyipa ndipo makamaka iwo amene sakumudziwa Khristu ndipo ndiwotsutsa kwambiri, mtumwi Paulo akunena kuti tikusowekera kukhala anthu amene sitingokakamira ku maufulu anthu. Mukusumbudzuka kwa moyo… ndi dziko lonyenga, lodzikonda la agalu kudya agalu. Kotero kodi Mkhristu akhale bwanji? Ngati ndikotheka, Iye akuti "Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzache." Ndiye kenako pali ntchito, pomwe mukudalitsa adani anu, mumayamba kuzindikira, ndichichita ichi ine. Ndilemba kadi. Ndikawawona kuchipatala. Ndidziwapempherera iwo tsiku ndi tsiku.

Mwina mungayambe kuganiza, ndine munthu wodabwitsa, wauzimu wosangalatsa wokonda dziko ili laufiti, amene anandithawa. Uwu ndi mtunda wa mawu otsutsana ndi akuti musadziyesere anzeru. "Onani, ichi ndi chovuta kwa ena mwa ife". Patsiku lina, chinthu chomwecho chimene munthu anachitira inu munthawi yanu yofooka ndi yopsinjika, mukadatha inu kuchitira ena.

Kotero sitikubwera ngati akulu oyang'anira. Tikubwera mogwirizana ndi kulumikizana ndi umunthu wathu, anthu amene ndi otsika udindo. Ndipo sitikuyerekeza koma ndi modzichepetsa kuti timawadalitsa iwo ndi nzeru za chisomo cha Mulungu, ndikadamachitira zinthu izo ena.

Izi zikumvekadi ngati Yesu, zoona? Pali njira imene yalambulidwa yakuti tiyitsatire. Ndipo kotero iyi ndi mbali yabwino. "Dalitsani iwo" - Ndipo dziwani- "iwo amene azunza inu." Iwo akusakasaka inu.

Lamulo lachiwiri ndi loyipa: musabwezere nokha. Ndime 17-20. Musabwezere choipa ndi choipa. Ndikutanthauza, ili ndi lamulo chabe. "Musabwezere choipa ndi choipa." Ndiye kenako akunena kuti "Samalani," Zungulizani mawu amenewa "Samalani". Kwenikweni, akutanthauza kuganizira modekha. Kumasulira kwa Baibulo la "The New American Standard" akuti, "Perekani ulemu kwa chimene chili cholondola mmaso mwa anthu onse. Ngati kungatheke, mmene zingatengere ndi inu khalani mwa mtendere ndi wina aliyense.

Ndiye kenako akupitirira kunena, tangodikirani pang'ono. Musabwezere mwa inu nokha koma patukani ku mkwiyo wa Mulungu. Iye ndi amene ali oweruza. Iye ndi amene apereka chilungamo. Mfundo ndi iyi. Kubwerezera ndi koletsedwa kwa anthu a Mulungu.

Mmawu ena, anachita choipa kwa inu, mudzalandilanso. Anachita choipa kwa inu kotero kuti inunso mmanena zinthu zoipa zokhudza iwo. Ndipo ngati muli Akhristu, ndipo munayamba mwakumana nazo kale, mungathe kuchita munjira zamavuvu koma zosaonekera. Mumaphatikiza malembo ku zimenezo ndi kuponyamo, "ndi chopempherera." Zimachitikadi, ndikhulupirireni.

Mumapita kuseri kwawo monga ngati chonchi, ndiye mumawabaya, chifukwa cholinga chanu chenicheni ndi kubwezera. Ndi malipiro. Mumagwiritsa ntchito mphamvu zanu, mumagwiritsa ntchito nzeru zanu, mumagwiritsa ntchito maubale anu, mumagwiritsa ntchito malingaliro ndipo mmalankhula chonchi. "Akangomwanso mankhwala oopsya , chonde. Udzamupha pompano kapena nthawi ina" koma sizitero ayi. Musadzabwezere choipa ndi choipa.

Mmalo mwake, lingalirani ndi kuganizira mmene anthu amaganizira ndi kuzindikira kuti iwo alibe chimene inu muli nacho. Iwo sangachitire monga mmene inu muchitira. Choncho musachite ngati iwo. Iwo

amangolunjika pa iwo eni okha. Lingalirani za mmene anthu amaganizira. Zidzakuthandizani inu kukhala mogwirizana ndi iwo.

Kubwezera nokha kukuletsedwa pa zifukwa ziwiri zofunikira. Choyamba, kumatenga udindo wa Mulungu ngati oweruza. "Kubwezera kuli kwanga." Mulungu akuti, Ine ndi wolungama. Inde, Ine ndi woyera, ine ndi wachifundo, ndimachedwa kukwiya, koma ndine wolungama. Ndipo mawu akuti chilungamo chinazikika mizu mu mmalingaliro. Mukudziwa, milingo ya chilungamo. Chilungamo chinazikika mizu mulingaliro lomveka bwino la kubwezera. Kubwezera mosavuta ndi uku. Pomwe mwachila zinthu zoipa pamakhala zotsatira zake zoipanso. Pomwe mwachita zinthu zabwino mumalandira mphotho. Munthu aliyense adzalandira chomuyenera.

Kotero kuti mukufunika kunena, kuti ndikusowekera kutenga mpira wa chiweruzo, ndikumupatsa Mulungu, ndikunena kuti ndatopa ndikuyeserera kutenga mpira wa chiweruzo, ndikumupatsa Mulungu, ndikunena kuti ndatopa ndikuyeserera kupeza njira za mmene ndingabwerere kwa bwana wanga, kapena kwa chibwenzi chakale, kapena ndi kwa mmodzi wa ana anga kapena kwa munthu amene anandichitira nkhanza. Ndipo ndidzayika mpira umenewo mmanja mwa Mulungu kuchokera pano mpaka muyaya. ndikunena kuti, "Mulungu, ndikukhulupirira kuti Inu ndinu wolungama kuti Inu mudzachita chimene ndi cholondola. Ine ndikutulukamo. Ndi zanu Mulungu. Ndikuzimasulira kwa Inu. Inu ndinu wosakondera. Inu ndinu wolungama." Ndipo mwina kumbali iyo ya kumwamba kapena kumbali iyo ya kutha kwa moyo, milingo idzakhala yoyenera mwamtheradi ndi yangwiro,

Mungathe kumasula chilonda chimenecho ndi chipweteko, ndi khumbo lanu lobwezera, chifukwa Iye amadziwa zinthu zonse. Iye amadziwa zifukwa zonse. Iye amadziwa zochitika zonse zozungulirapo, ndi inu simungathe, ndipo mungathe kumupatsa izi kwa Iye. Koma ngati mungalamule kukhala oweruza, ndipo Mulungu sangakhale oweruza. Ndipo pomwe muweruza anthu, ndipo mwapanga chiganizo chakuti mudzawabwezera iwo, mumakolola zimene munafesa.

Chifukwa chachiwiri chimene kubwezera ndi koletsedwa ndi chakuti ndi njira yopanda mphamvu yobweretsera mtendere. Tayang'anani ndime iyi ndi kangati kamene ikunena za umodzi, ndi wina ndi mnzake, ndi kukhala mogwirizana. Mulungu amafuna ife tidzikhala mdziko lakugwa ndi loyipa pomwe ife tili anthu amene timabweretsa mtendere, ndipo sitikakamira ku maufulu athu.

Ndife mtundu wa anthu olembedwa ntchito amene anthu amanena kuti Eeeh, tikufunika tilembe ntchito anthu ena zana okhala ngati iwo chifukwa a ntchito ena kukonda miseche, izi ndi izo, ndikufuna izi ndikufuna izo ndi anthu ovuta kwenikweni. Koma ine ndimakonda Akhristu awa. Amapanga kampani iyende bwino. Ndi okonda, ndi osadzikonda ndi osamala. Sakhala ngati zopondera ukamalowa pakhomo. Uwu simtendere pa mtengo uliwonse. Amayimirira pa mfundo. Amayimirira pa khalidwe loona. Simungathamangitsane nawo. Koma ndi anthu okhulupirika amabweretsa mtendere. Mukufuna awa mugulu lanu. Mukufuna iwo akuthandizeni - mukudziwa, kuyendetsa zinthu za kampu ya malo a zinthu zosangalatsa. Ndi qnthu abwino.

Ndiye pomwe akwiyitsidwa, sakhala osakhazikika kuti nthawi zonse amayambitsa mavuto. Amawayang'ana anthu ndi kulingalira za komwe munthu winayo akuchokera, Amaganizira kuti mwina mwake ndiwapempherere iwo. Sitiyambitsa mavuto. Tipanga malo ano kukhala abwino kwambiri.

Mukumvetsetsa? Pomwe mwabwezera choipa kwa choipa, choipa kwa choipa, mukudziwa monga mmene zilili? Kuli ngati moto ukuyaka pang'ono kuli ngati kutenga, mpopi umodzi waukulu othimizira moto wa

anthu ozimitsa moto ndiye mmalo mwa madzi kutuluka, mukutsira mafuta. Ndipo ichi ndi chimene anthu amachita. Amachita izi mmabanja awo, amachita izi mmaukwati awo, amachita izi za alamu awo, amachila izi ku ntchito zawo. Amachita izi. Anachita icho. Tinachita ichi.

Nthawi ina yake mkati mwasabatayi, mukhale pa malo pa chigulugulu, ndi kumvetsera anthu ena ndi kuwona zokambidwa - ndikubetchelani zili mma 80 pa 100 - ndi za wina wake amene sali patebulo. Koma amayi anu anachita icho, ndi kuchita icho, sindingakhulupirire mlongo wako, ndipo anachita icho. Ndipo mukudziwa Bob ndi amene ndi bwana? Kodi mungakhulupirire iwo akuchita izi ku ntchito? Zoona?

Ndiye kenako amanyamula maganizo awa, amawononga moyo wawo omwe. Ndikunena kuti ndi zoona kwa ambiri mwa ife, ndipo Paulo akunena kuti osachita zimenezo. Zilibe mphamvu. Pamenepo, akulowera kwakuya ndipo akunena kuti, pamenepo, ngati mdani wanu, munthu amene anakupwetekani inu, ali ndi njala - athandizeni iwo. Apatseni iwo chakudya, ngati ali ndi ludzu, apatseni chakumwa. Mukachita choncho, mumawawunjikira makala a moto pa mutu wawo.

Chinthunzithunzi ichi choyatsa makala sichofuna kukupwetekani monga ndanena kale. Unali mwambo wa ku Egypt mu nthawi imeneyo. Ancient Near East. Ngati munthu mu miyamba imeneyo wazindikira kuti akwiyitsa munthu wina panali mkangano ndipo iwo ndi wolakwa, ndiye amakoleza moto, ndi kutenga makalawo kuwachotsa pamoto ndi kuwayika pa phale. Ndiye kenako amatenga mpango, ndi kuwuyika pansi pa phale, ndiye kenako amayika pa mutu pawo, ndiye amayenda kuzungulira mudzi onse ngati chizindikiro cha, “ndikuyatsa maganizo anga oyipa mmoyo mwanga. Ndinalakwa.” Tingathe kugwiritsa ntchito mawu akuti ndalapa. Ndasitha maganizo.

Ichi ndi chimene mukuwona chikuchitika mu Malemba. Ichi ndi chimene mumachita chabwino kwa anthu, ndipo amadziwa kuchokera pansi pa mitima yawo ndi chimene mumachita chabwino kwa anthu, ndipo amadziwa kuchokera pansi pa mitima yawo ndi mmaganizo awo kuti sakuyenera icho. Zimabweretsa manyazi, ngakhale mwa anthu oyipa. Ichi ndi chinthunzi cha Davide, ndipo Davide amathawitsa moyo wake. Ndipo chili chonse chimene anachita ndi kugonjetsa adani kunkhondo, ndi kusamalira Sauli ndi kusamalira Mfumu ya Israel amene anali Sauil. Ndipo Sauli anayesetsa ndi mtima wake wonse, ndipo anamuthamangitsa David ndi kuyesetsa kumupha iye. Mukudziwa nkhaniyo?

Ndiye kotero, akuthamanga, kuthamanga, kuzemba, kuzemba. Mapeto ake, iye anazungulilidwa, ndi iye anapezeka muphanga. Iye anyamata ake ali mkatikati mwa phangalo ndipo Sauli wawazungulira, ndipo kuli ngati anyamata, nthawi ija ndi ino. Titha ngati angatipeze. Ndipo chodabwitsa, Sauli akulowa mu phangamo, ndipo Baibulo likupereka chojambula… Iye akudzithandiza iye mwini yekha Ndipo sindikudziwa, mwina mwake anagona atamaliza. Sindikudziwa makamaka kuti zonse zimachitika bwanji. Baibulo silikunena. Koma anzake a Davide akuti Mulungu watipatsa iye kotero tsopano mubwezere inu pa Sauli.

Ndipo David anamvetsetsa udindo wake. Davide akuti, ine siine oweruza. “Sindidzakhudza odzozedwa wa Ambuye.” Anzake amanena kuti Mulungu wamubweretsa muno. Ili ndi yankho la pemphero. Mupheni. Davide akuti ayi, ayi. Koma akuyandikira Sauli, kutenga mpeni, ndi kung’amba kachidutswa pansi pa chovala chake. Sauli akutuluka muphanga, akutsika muchigwa, kupita kumbali ina yachigwa ndipo Davide akutuluka kukamwa kwa phanga. “Sauli, Sauli chifukwa chiyani? Ndinachita chiyani? Mulungu anakubweretsani ku phanga.” Iye anakweza mkwawo wa mwinjiro ndi kunena kuti, “Onani mwinjiro wanu. Ndikanatha kukuphani.” Ndiye kenako akuyankhula mawu awa osangalatsa. “Chifukwa chache Yehova

akhale woweruza pakti pa ine ndi inu. Ngati muli woulungama koposa ine, ndivomereza udindo wonse. Koma Mulungu anditulutsemo. Koma ine ndachita chotani?

Onani, anapereka chabwino mmalo mwa choipa. Ndiye kenako, mosangalatsa Sauli akuyamba kulira. Kukhala ngati mukuthwanima, mukamphindi aka, wazindikira choonadi. Onani, pomwe anthu akuchita zinthu zoipa, amazikankhira pansi, kenako amakhala moyo okana. Ndiye pa zinthu za ziwanda zimene zimachitika ndi anthu amene mopitiriza amachita zinthu zoipa mpaka pamene saganizanso kuti zimene akuchita ndi zoyipa ndipo zimafika pa chizolowezi chokanika kusiya. Ndipo iyi ndi nthawi ya chisomo, Saul akulira ndi kunena kwa Davide, iwe ndiwe wolungama kuposa ine. Ndiye mwatsoka ilo, ndi kulapa kwakufupi, ndi kulapa kosakhalitsa.

Koma mungathe kulingalira zimene zingachitike ngati aliyense muchipinda chino anganene kuti, “Mulungu, mudzi wathu ungafikiridwe, mwina mwake sangakhale madongosolo a chipembedzo omwewomwewo kapena maumboni ena atatu a za mmene ife tili opambana, ndipo tikufuna kumuthokoza Yesu chifukwa ndi amene anapanga zonse.” Zinthu izi zili bwino, koma nanga bwanji titakonda adani athu?

Nanga bwanji ngati mutayenda muzitseko zina, ndipo mwaganiza kuti ndimukhululukire makamaka munthu uyu, ndipo bwanji mutayamba ulendo wowapempherera iwo? Mwina mwake mosadzidziwitsa kuwachitira china chake iwo kungowadalitsa. Mwatsoka, tili ndi chizolowezi chowanena kuti ndi ziwanda anthu amene anatipweteka ife. Kodi munazindikira ichi? Chifukwa chakuti anatipweteka kwambiri, chilichonse chimene timachita ndi chabwino, ndiye nkhani yonse timayikonzanso.

Nkhani zambiri zimakhala zosemeka bwino. Sizikutanthauza kuti sanachite china chake choyipa kwambiri. Koma chingachitike ndi chiyani ngati mmidzi yathu tingakonde adani athu? Ngati tingawadalitse iwo? Ngati tinganene, “Mulungu, mukhale oweruza.” Ngati tingakhale omasuka. Chabwino, pano pali chotsatira chozizwitsa - chabwino kugonjetsa choipa.

Tsopano ndazindikira kuti ena mwa inu mungamaganizire kuti, “Simukumvetsetsa kwenikweni. Mwina simungamvetsetse chimene ine ndadutsamo. “Ndipo mukudziwa chiyani? Sindikudziwa. Koma maphunziro ena amene mmaphunzira nthawi zina mmoyo, ndipo ena moyambirira, ndipo phunziro limene ndinaphunzira ndili Mkhristu wachichepere munjira yamphamvu kwambiri ndi imene inawumba tsogolo langa.

Ndinadziwa Khristu mu chirimwe ndi angochoka kumene ku sekondale sukulu. Ndinapita kukasewera basketball yolipilidwa ndi sukulu. Ndinali wa chaka choyamba ndipo ngati ndingasewere bwino, ndikadakhala nawo mutimu imene imayenda. Munthu wina anabwera amene anatengedwa ngati chiphona cha timu. Anali atakhalako ku ndende nthawi ina yake, anayenera kukhala munthu amene wasinthidwa moyo wogwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo ndi wogulitsa mankhwala. China chake chinachitika mmoyo mwake sindikudziwa kaya ndi mmene analeledwera, koma amadana ndi Akhristu. Sindikutanthauza kuti sanawakonde, anawada Akhristu.

Munthu uyuyu anazindikira kuti ine ndine Mkhristu, ndipo anayamba kumandiseka ndi kumandinyoza pa chilichonse kuphatikizira chikhulupiriro changa. Ndipo ngakhale kundigwira thupi kamodzi ndi kundiwopseza kuti adzandipha. Ndinachita mantha akulu chifukwa munthu uyuyu anali wowopseza kwambiri. Ndinali wodandaula nthawi zonse ndipo sindimatha kugona usiku, ndipo ndinayamba kukhala ndi mkwiyo. Ndinali ndi mkwiyo weniweni. Monga ngati kuchita china chake chimene chidapereka chisoni mmoyo wanu wonse.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

Mkwiyo unalamulira moyo wanga, ndiye panali munthu wina amene ndinali naye mu gulu losanthula Baibulo ndipo ndi nagawana naye nkhani yonse. Iye anati, “Mukufuna chithandizo?’ Ndinanena, “Kumene ndikufuna chithandizo!” Iye anati, “Cchabwino, chimene ndikuwuze iwe ndi chovuta kwambiri, koma ndikukutsimikizira kuti chigwira ntchito.” Ndinati, ”Inu ndidzachita chilichonse”. Ananyamula Baibulo anatsegula Aroma 12, anawerenga ndime 14 mpaka 21, ndipo iye anafotokoza zimene ndangokufotokozeranizi. Ndipo ndinamuyang’ana ngati, kodi wasuta iyeyu? Ndimudalitse munthuyu. Ndikufuna ndimuwombere.

Iye anati, “Mwanena kuti mukufuna.” Ndipo anati, “sizakumva, ndi chisankho kotero pa tebulo ili, tsopano lino, mukuyenera kumukhululukira iye chifukwa Mulungu akufuna amukhululukire iye.” Ndinati , “Sindikuganiza kuti Mulungu…… chabwino, eya, chabwino. Eya, ndikutsimikiza kuti Mulungu akufunadi kumukhululukira iye. Ine sindingofuna. Ndipo mwakufuna ndasakha kumukhululukira iye.” Ndipo iye anati, “Tsopano, mukusowekera kumudalitsa iye.” Kotero, ndinamupempherera iye tsiku lililonse ndi kuyamba kumudalitsa iye paliponse ndingapeze mwayi otero.

Ndipo patatha mwezi kapena ingapo, anati, “Ukuyesera misampha ina ya Chikhristu pa ine?” Ndinati, “Ayi, Yesu anati ndiyenera kukonda aliyense, ndipo ine ndikuyesetsa kuchita mbali yanga yabwino kwambiri.” Chabwino, ndikufuna ndinene kuti, iyi ndi mwa nkhani izo zomwe miyezi iwiri ndi theka, analowa mu kabathi, kugwada pansi – “Oh, Yesu, chonde ndikhululukireni.” Nkhani sikuthera pamenepo. Chabwino, chifukwa imeneyo sinkhani yake.

Miyezi iwiri, miyezi itatu, palibe chinasintha. Nthawi zonse amandinyoza. Kupatula chinthu chimodzi. Patatha mwezi izi zitachitika, ineyo ndinasintha. Chidani changa chinatha. Mantha anga anatha. Ndinatuluka mundende ndinaona kuti munthuyu anali wanzeru. Anali waluso lodabwitsa.

Ndipo ndinafika pakuti ndinanena kuti ndikudabwa ndi chimene chinamuchitikira munthu ameneyu, kumene amachokera, ndi kumene wakhala akukhala? Ndinalibe chidziwitso cha zimene iye wadutsamo, ndipo ndinalibe chidziwitso cha mmene Akhristu ena anamuchitira. Zonse zimene ndimadziwa pa nthawi iyi ndi zakuti ndinafika pa mfundo imene ndinasamaladi za iye. Chifukwa chiyani? Ndinamudalitsa iye. Ndinamupempherera iye. Ndinachita bwino. Ndipo mukachita choncho. Mulungu amachita china chake mwa inu.

Pakutha pa nyengo, iye anatembenukira kwa ine, ndi kuti “Chiiiipi. “Ine ndinati eee?” Ie anati, “Ukudziwa, pali anthu awiri okha amene ndimalemekeza mu timu yonseyi. Ndakhala ndikuseweretsa maganizo a anthu awa. “Iwowo ndi zinyalala.”

Anati, “Ine, chifukwa ndine woipa, ndipo ndimadziwa ichi, ndipo ngati kuli gahena, ndikupita kumeneko. Ndipo iwe, chifukwa chakuti sindigwirizana ndi chili chonse chimene iweyo umayimirira, komanso umakhala moyo wake. Ndipo sindifuna mkomwe, kukhala Mkhristu, koma ngati ndingaganizireko kuti ndikhale, ndikhoza kukhala ngati iweyo.” Ndipo anati, ”Ukudziwa chiyani? Ndathana nawe sizosangalatsanso kukuvuta iwe. Kotero wamaliza, tuluka muno Chiiipi.”

Ndiye pano pali chimene ndikufuna kukuwuzani. Mulungu akufuna kuti inu mukonde adani anu kuchitira inu ubwino, ndi kuchitira ulemereno Wake.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge